# ASSEMBLY FOR ALL NATIONS INTERNATIONAL MINISTRIES

# MALAMULO A MPINGO WA PAMALO

**LILONGWE, MALAWI**

**November 2023**

# Za Mkatimu


| Gawo | Mutu |
|---|---|
| 1 | Dzina |
| 2 | Matanthauzo |
| 3 | Mpingo wa pamalo |
| 4 | Akazi a Busa |
| 5 | Malamulo a Khalidwe |
| 6 | Mwambo |
| 7 | Kasinthidwe Ka Malamulo |

# MALAMULO A MPINGO WA PAMALO

Kolingana ndi Malamulo ndi Mayendedwe a Assembly for All Nations mipingo yonse imene ili pansi pa Assembly for All Nations idzachita zonse motsogozedwa ndi malamulo a mpingo wa pamalo ndi cholinga choti pakhale cholinga chimodzi, makhalidwe ndi machitidwe ofanana. Pokhala mpingo wokhulupilira za Mzimu Woyera (Pentecostal) mpingo uliwonse wa pamalo udzakhala ndi cholinga chofalitsa uthenga mwa mphamvu ya Mzimu woyera, kuti ukapange mipingo yanzika, ndipo kuti ikatsate fundo zonse za Assembly for All Nations.

## GAWO 1

## DZINA

Mpingo uli wonse, utavomerezedwa ndi Bungwe la pamwamba mdziko liri lonse (NEC), ungathe kugwiritsa ntchito dzina lili lonse pansi pa dzina lalikulu la Assembly for All Nations (Gawo 1, Ndime 3 yamalamulo a AFAN).

## GAWO 2

## MATANTHAUZO (Gawo 2, Malamulo a AFAN)

i. **Bungwe la Adindo Dziko lonse** (AfAN Global Board). Ili ndi bungwe la adindo khumi ndi awiri omwe adzayendetsa ntchito za mpingo wa Assembly for All Nations pa dziko lonse lapansi. Bungweli lidzayendetsanso ntchito za Msonkhano wa azibusa onse (Global Pastors Conference) omwe amatsogolera AfAN (National Pastors) mu mayiko onse komwe mpingowu ukatsegulidwa.

ii. **Msonkhano Waukulu** wa onse umene mapangidwe ake alongosoledwa mu Gawo 9, ndime 2 ya malamulowa ukutanthauza gulu la nthumwi zoyitanidwa zomwe zidzakhala ndi mphamvu ndi ulamuliro koposa onse mu Assembly for All Nations.

iii. **Mpingo wa AfAN** m'dziko liri lonse udzatchedwa (National Church).
Ili ndi dzina lomwe lidzatchulidwa nthawi zina mmalo mwa Assembly for All Nations m'dziko liri lonse lomwe kudzakhale mpingowu.

iv. **Adindo a mpingo M'dziko** (National Officers).
Awa ndi akuluakulu womwe adzayendetsa mpingo m'dziko liri lonse.

v. **Bungwe la Adindo a Mpingo m'dziko** (National Board of Administration)
Iri ndi bungwe la adindo asanu ndi mmodzi a mu ofesi ya pamwamba amene adzayendetsa ntchito za msonkhano waukulu wa onse m'dziko (General Assembly), msonkhano waukulu wa Atsogoleri (General Presbytery) ndi Bungwe la pamwamba m'dziko (National Executive Committee) pamene sakugwira ntchito.

**vi. Ofesi yayikulu m'Dziko (National Office)**
Iyi ndi ofesi ya pamwamba kumene ntchito za Atsogoleri (Adindo akuluakulu mu Mpingo m'dziko liri lonse) amagwirirako ntchito mmalo mwa mpingo m'dziko (National Church).

vii. **Bungwe la pamwamba m'dziko (National Executive Committee)**

Ndi bungwe Loyang`anira ntchito zonse za mpingo m'dziko.

**viii. Msonkhano wa ukulu wa Atsogoleri (General Preysbtery)**

Iri ndi gulu la atsogoleri lomwe ndi lachiwiri mu ulamuliro mu Assembly for All Nations m'dziko liri lonse. Gululi limapangidwa ndi atsogoleri wochokera ku Bungwe la pamwamba pa dziko lonse lapansi (Global Board), bungwe lapamwamba m'dziko (National Executive Committee), Mabungwe a m`zigawo Za zikulu (Division Committee), Mdindo wa chigawo (District Director), Adindo a mautumiki (National Ministry Directors) ndi Adindo a Ma dipantimenti (Heads of Departments).

**ix. Chigawo Chachikulu (Division)**

Ichi ndi chigawo cholamulidwa cha mpingo m'dziko chimapangidwa ndi maboma angapo ndipo mtsogoleri wake amatchedwa (Director)

**x. Chigawo (District)**

Ichi ndi chigawo cholamulidwa cha mpingo m'dziko. Malire amabomawa nthawi zina adzasatana ndi malire a maboma a dziko la Malawi koma nthawi zina mpingo uli ndi ufulu woyika malire ake movomerezedwa ndi msonkhano waukulu wa Atsogoleri (General Assembly).

**xi. Msonkhano wa Chigawo (District Assembly)**

Uwu ndi msonkhano umene uli ndi mphamvu za pamwamba mchigawo (District).

**xii. Oyang`anira wa chigawo (District Director)**

Ndi mkhala pa mpando ndi mtsogoleri wa chigawo chonse.

**xiii. Dera (Cluster)**

Boma lidzagawidwa m`madera ang`ono ang`ono amene adzakhala ndi ma udindo woyendetsa ntchito za mmaderawo. Madera adzakhala ndi udindo woyang`anira mipingo ya pa malo angapo.

**xiv. Woyang`anira Dera (Cluster Director)**

Ndi mkhala pa mpando ndi Mtsogoleri wadera.

**xv. Mpingo wa pamalo.**

Iri ndi gulu la okhulupilira amene amasonkhana monga mpingo wa pa malo kukwaniritsa cholinga cha Assembly for All Nations.

**xvi. Mipingo ya nzika ya Utumwi (Indigenous Missionary Churches).**

Iyi ndi mipingo ya pa malo imene imadzilamulira yokha; Imadzithandiza yokha; komanso imadzikulitsa yokha. Ilinso ndi udindo obzala mipingo ina yochita chimodzi modzi.

**xvii. Zigawo za mpingo**

Ndi mabungwe omwe amagwira ntchito zina ndi zina zothandiza mpingowu monga za umoyo, maphunziro, kuthandiza pa mavuto ndi chitukuko.

**xviii. Mautumiki a mpingo**

Awa ndi mabungwe amene amagwira ntchito zimene ziri zolinga zeni zeni za Assembly for All Nations

**xix. Ntchito za Ulangizi.**

Izi ndi ntchito zimene zimachitka ndi Abusa amene adapuma. Abusa okhalitsa, komanso ogwira zintchito zina amene angafunsidwe kupereka uphungu kwa Abusa amene akugwirabe ntchito.

**xx.** **Bwalo la Likulu pa dziko lonse (Global Disciplinary Council)**
Iri ndi bwalo la pamwamba komanso lomaliza pa dziko lonse lapansi loweruza milandu la Assembly for All Nations.

**xxi.** **Bwalo la Likulu m'dziko (National Disciplinary Council)**
Iri ndi bwalo la pamwamba m'dziko liri lonse loweruza milandu la Assembly for All Nations.

**xxii.** **Bwalo lachiwiri (General Disciplinary Committee)**

**xxiii.** **Atsogoleri a Mautumiki M`dziko liri lonse (National Directors of Ministries)**
Awa ndi anthu amene ali ndi udindo wotsogolera ndi kuyang`anira ntchito ndi zochitika m`mautumiki a mpingo.

**xxiv.** **Mpingo Wokhulupilira za Mzimu Woyera (Pentecostal Church)**
Iri ndi dzina lomwe limagwiritsidwa ntchito kufotokozera mpingo wa dziko lonse kapena mpingo wa pa malo umene machitidwe ake ndi makhalidwe ake amagwirizana ndi mpingo wa m`chipangano chatsopano. Umakhulupilira Ubatizo, kudzazidwa ndi kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera za utumiki m`nyengo ino. Komanso umakhulupilira kuti chizindikiro choyamba chooneka ndi maso chakudzazidwa ndi Mzimu Woyera ndi kulankhula m`malilime ena.

## GAWO 3

## MPINGO WA PAMALO

**Ndime 1 - Khalidwe:**

Gulu la okhulupirira limene limakumana nthawi ndi nthawi kupembedza, ndipo ndi gawo la Dera (Cluster) komanso limatsatira mfundo ndi ziphunzitso za Assembly for All Nations lidzazindikirika kuti ndi mpingo wa pamalo ndipo udzakwaniritsa zoyenera izi: (Gawo 11, Ndime 2 ya Malamulo a AFAN)

i. Mpingo wa pamalowo udzakhala ndi mndandanda wa anthu amene amasonkhana pa mpingopo mosajomba kwa miyezi 6.
ii. Mpingo udzathandiza m`busa wawo kuchokera mu chachikhumi, zopereka za mamembala a mpingowo ndi ndalama zina zimene zingapezeke mwa njira zina.
iii. Padzakhala Akulu a mpingo amene adzakhala ndi zowayenereza kolingana ndi malamulo ndi mayendedwe a Assembly for All Nations ndi malamulo a mpingo wa pamalo.
iv. Mpingo udzakhala ndi ma utumiki ndi ma bungwe wogwira ntchito awa:
   a) Sukulu ya Baibulo
   b) Utumiki wa amayi
   c) Utumiki wa achinyamata
   d) Utumiki wa abambo
   e) Utumiki wa Ana
   f) Utumiki wa usodzi ndi utumwi
   g) Bungwe lothandiza zosowa, maphunziro ndi chitukuko.
   h) HIV/AIDS ndi zaumoyo

i) Milaga (Homecells)

j) Mpingo wapamalo udzathandiza wophunzira womwe ali kusukulu ya Abusa yovomerezeka ndi Assembly for All Nations popereka malipiro onse kapena mothandizana ndi ophunzirayo kolingana ndi kuthekera kwa mpingowo komanso kuwathandiza m`Madera ena.

v. Mpingo wa pamalo udzakhala ndi nyumba ya Abusa kapena kuwapezera abusa nyumba yokhalamo komanso nyumba yopemphereramo yosamalidwa bwino. Mpingo udzalipilira nyumba abusa ngati mpingowo ulibe nyumba yokhalamo abusa pa mpingopo.

vi. Mpingo udzathandiza abusa ndi ndalama zothandizira banja lawo (monthly allowance) komanso ndi zithandizo zina ndi zina monga za ma homecell, airtime komanso mayendedwe popita ku misonkhano ya mpingo.

vii. Mpingo udzayembekezeka kukula moyo wa Uzimu, m`chiwerengero ndi mchuma.

**Ndime 2: Okhala mu Mpingowu**

Mpingo wa pamalo udzakhala ndi awa:

i. Abusa amene ali ovomelezeka ndi bungwe lalikulu la AfAN (Global Board).
ii. Akulu a mpingo osankhidwa ndi m'busa wa pa mpingopo.
iii. Mamembala ovomerezeka malingana ndi malamulo a mpingo.

**Ndime 3: Udindo wa mpingo wa pamalo**

Udindo wa mpingo wa pamalo ndi kuchita komanso kukwaniritsa zolinga za Assembly for All Nations zimene zili m`munsimu:

i. Kulimbikitsa ndi kuthandizira kufalitsa uthenga wabwino kudziko lonse lapansi.
ii. Kulimbikitsa ndi kuthandizira kulambira Mulungu Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, mu Mzimu ndi m`choonadi.
iii. Kulimbikitsa ndi kuthandizira okhulupilira onse.
iv. Kupereka mwayi wachiyanjano kwa akhristu achikhulupiriro chofanana.
v. Kulimbikitsa kuthandiza osowa.

**Ndime 4: Zochitika za padera pa mpingo wa pamalo**

Mpingo wa pamalo udzachita nawo zinthu zonse zimene Assembly for All Nations yayika pa ndondomeko yake ya pa chaka motere:

***i. Tsiku lothokoza Abusa:***

Ili ndi tsiku limene mpingo umathokoza abusa chifukwa cha ntchito imene akugwira pa mpingopo. Mpingo udzakonza mphatso ndipo zidzaperekedwa kumapeto kwa ulaliki, mautumiki komanso anthu ena pa okha adzapatsidwa mwayi wopereka mphatso zawo. Tsikuli silikulowa m`malo mwa tsiku limene mpingo umapereka mphatso za kwa abusa.

ii. ***Masiku ena Apadera:***

Padzakhala tsiku la: Utumiki wa Ana, utmiki wa amayi, utumiki wa Abambo, utumiki wa Achinyamata, Usodzi ndi Utumwi, komanso masiku ena amene bungwe la pamwamba dziko lonse lapansi (Global Board) lingakhazikitse.

Pa masiku apaderawa chopereka chapadera, pambali pachopereka chatsikulo chimene chimatsala pa mpingo, chidzalandilidwa kuti chikathandize ofesi yayikulu ya utumikiwo.

**Ndime 5: Mlingo wa umembala wa mpingo**

Mpingo uli wonse udzakhazikitsa tsiku lolandira ma membala atsopano.

Mamembala onse atabatizidwa adzakhala pa maphunziro kuti awonetsere kukhulupirika kwawo komanso kuti aphunzitsidwe ziphunzitso zazikulu za Assembly for All Nations ndi ziphunzitso zina zokhudzana ndi chikhalidwe choyenera ndi udindo wa okhulupirira.

**Zoyenera Umembala ndi Izi:**

i. Kubadwa mwatsopano
ii. Kubatizidwa m`madzi
iii. Kuyenda moyo wachiyero
iv. Kukhulupirika kukhala nawo pa mapemphero
v. Kupereka chachikhumi pa ndalama zonse zimene wokhulupirirayo amalandira asanachotsepo zina ndi zina.
vi. Kukhulupirika ku chiphunzitso ndi mfundo za Assembly for All Nations.
vii. Kumaliza bwino bwino maphunziro a umembala

**Ndime 6: Zoyenera munthu kuti akhale Mkulu wa Mpingo kapena Mtumiki**

i. Akhale wobadwa mwa tsopano
ii. Akhale wobatizidwa m`madzi
iii. Akhale wobatizidwa ndi Mzimu Woyera ndi chizindikiro cholankhula ndi malilime ena.
iv. Akhale wokhulupirika popereka chachikhumi, zopereka, ndi zopereka zina zonse za pa mpingo.
v. Akhale wokhulupirika kumapemphero ndi misonkhano ina yonse
vi. Akhulupirike ku ziphunzitso ndi zikhulupiriro za Assembly for All Nations.
vii. Akhale moyo wachitsanzo ndi wopanda mbiri yoyipa.
viii. Akhale membala wovomerezeka wa mpingowo.
ix. Akhale wokonzeka kukhala pansi pa ulamuliro wa m`busa wamkulu ndi abusa onse apa mpingopo.

**Ndime 7: Bungwe la Akulu a Mpingo (Church Council)**

Pa Mpingo uli wonse wa pamalo padzakhala bungwe la akulu a mpingo (church council) m`mene mudzakhala:

i. M`busa wamkulu
ii. Abusa onse othandizana naye amene adzasankhidwa ndi mbusa wamkulu
iii. Woyendetsa ntchito, Mlembi, Wachiwiri kwa Mlembi, Msungi chuma, woyendetsa ntchito za Milaga ndi atsogoleri ena a ma utumiki kapena mabungwe.

**Ndime 8: Kusankha Akulu a Mpingo ndi Atumiki**

i. Akulu a Mpingo kapena Atumiki adzasankhidwa ndi m`busa wa mkulu kuti agwire ntchito chaka chimodzi kapena zaka ziwiri. Akulu a mpingo kapena Atumiki angathe kusankhidwanso ngati achita bwino pa ntchito yawo.
ii. Mkulu wa Mpingo kapena Mtumiki angathe kuchotsedwa pa udindo ngati akulephera kugwira ntchito yake kapena sakulimbikitsa masomphenya a m`busa wamkulu.

**Ndime 9: Ntchito ya Bungwe la Akulu a Mpingo**

Bungwe la Akulu a Mpingo lidzagwira ntchito Izi:

i. Kulimbikitsa, kuchenukitsa ndi kuwirikiza masomphenya a m'busa wamkulu.
ii. Kulimbikitsa kuthandiza abusa moyenera popereka thandizo lokwanira losamalira banja lawo, nyumba yogonamo yabwino, ndi zinthu zina zonse zothandizira ubwino wa abusa komanso kupereka ndalama zozapumira abusa pa ntchito yawo (pension).
iii. Kuonesetsa kuti malo wopempherera ndi owoneka bwino komanso osamalidwa bwino.
iv. Kuonesetsa kuti ma utumiki onse akugwira ntchito mogwirizana ndi masomphenya abusa.
v. Kuonesetsa kuti mpingo ndi abusa ndi wotetezedwa.
vi. Alandire malipoti wochokera ku ma utumiki onse.
vii. Afufuze ndi kuvomereza anthu amene afuna kuti akhale ma membala.

**Ndime 10: Bungwe loyendetsa ntchito za mpingo (Board of administration)**

Bungwe loyendetsa ntchito za mpingo lidzakhala ndi anthu awa:

i. Mbusa wamkulu (Lead Pastor)
ii. Abusa wothandizana naye ngati alipo (Executive Pastor)
iii. Woyendetsa ntchito (Administrator)
iv. Mlembi (Secretary)
v. Wachiwiri kwa Mlembi (Deputy Secretary)
vi. Msungi chuma (Treasurer)
vii. Oyendetsa ntchito za milaga (Homecell Coordinator)

**Ndime 11: Ntchito za Bungwe loyendetsa Ntchito za pa Mpingo**

Bungwe loyendetsa ntchito za mpingo lidzagwira ntchito Izi:

i. Kuonesetsa kuti ntchito za tsiku ndi tsiku za mpingo zikuyenda bwino.
ii. Adzapereka maganizo kwa abusa m`mene akuganizira kuti ntchito iyendere komanso dongosolo la kalowedwe ndi kagwiritsidwe ntchito ka ndalama za mpingo.
iii. Kulemba ndi kuchotsa anthu wogwira ntchito pa mpingo, motsogozedwa ndi abusa.
iv. Kuganizira ndi kukonza malipiro a abusa ndi anthu ogwira ntchito pa mpingo. Bungweri lidzafotokozera za izi ku bungwe la akulu a mpingo.
v. Kutsogolera pokonza mfundo za chitukuko cha mpingo m`mayendedwe, m`chuma, ndi anthu wogwira ntchito.
vi. Kumva ndi kupanga ziganizo pa milandu.
vii. kukhazikitsa ndondomeko ndi mfundo za kayendetsedwe ka mpingo.

***M`busa wa pa mpingo akamwalira bungweri lidzachita izi:***

a. Lidzakonza dongosolo la maliro pamodzi ndi atsogoleri a mpingo
b. Lidzalora kuti banja la abusa likhalebe pa mpingo kwa miyezi isanu ndi umodzi.
c. Lidzapereka thandizo kwa otsalayo limene mbusa amalandira kwa miyezi itatu.
d. Lidzathandiza kuti ndalama zimene zimasungidwa kuthumba la abusa (Ministers Benefit Fund) ziperekedwe kwa otsalawo.
e. Lidzakonza mayendedwe a otsalawo kupita kumudzi kwawo kapena kumalo komwe azikakhala.

**Ndime 12: Ntchito za Adindo a Mpingo**

***i. Mbusa wamkulu***

Ulamuliro woika mbusa wamkulu pa malo udzakhala m`manja mwa Dera (Cluster), chigawo (District), chigawo chachikulu (Division) kapena bungwe la pamwamba la dziko lonse (NEC). Mabungwewa adzakhalanso ndi mphamvu yosuntha mbusa wamkulu kupita ku mpingo wina.

Mbusa ayenera kupezeka pa mpingo kosachepera katatu pa mwezi ngati palibe zomulepheretsa kutero, ndipo adzagwira ntchito izi:

a. Adzakhala ndi udindo wosankha Akulu a mpingo.
b. Adzakhala ndi udindo pa moyo wa Uzimu wa mpingo.
c. Adzatsimikiza ndi kukhazikitsa cholinga cha mpingo.
d. Adzakhala woyang`anira ntchito yonse ya mpingo.
e. Adzapereka masomphenya a mpingo ndi kupereka dongosolo lakufikira masomphenyawo.
f. Adzakhala m`khala pa mpando wa misonkhano yonse ya mpingo. Akulu a mpingo asapange msonkhano ngati abusa a akulu sakudziwa.
g. Adzakhala membala wa mabungwe onse woyendetsa ntchito za mautumiki apa mpingo koma sadzaponya nawo mavoti nthawi ya zisankho.

h. Adzakhala wosayina makalata onse wokhudza malamulo a boma, komanso mabanki pokhapokha atapatsa udindowu kwa wina.

***ii. Mbusa wothandiza (Executive Pastor)***

Mphamvu yakuyitana kapena kuchotsa mbusa wothandiza ili mmanja mwa m'busa wamkulu pa mpingo wa pamalo. Mbusa wamkulu adzakhala ndi mbusa wothandiza monga mbusa mnzake amene ayenera kupatsidwa ulemu. Tsono ntchito ya mbusa wothandiza ikadzakhala kuti sikufunikadi pa mpingopo, mpingo udzamuthandiza mbusayo mpaka atapatsidwa mpingo. Abusa othandiza adzachita ntchito izi:

a. Adzakhala wachiwiri kwa mbusa wamkulu.
b. Adzagwira ntchito zimene angapatsidwe ndi mbusa wamkulu nthawi ndi nthawi.

***iii. Woyendetsa ntchito (Administrator)***

Woyendetsa ntchito adzagwira ntchito izi:

a. Kuyendetsa dongosolo la mpingo mmalo mwa abusa pamene abusa onse achokapo kapena ngati awuzidwa kutero ngakhale abusawo alipo.
b. Adzakonza komanso adzapereka malipoti ake mpingo.
c. Adzagwira ntchito zomwe zili mu Church Leadership Manual.

***iv. Mlembi (Secretary)***

Mlembi adzagwira ntchito izi:

a. Adzasunga mbiri ya misonkhano yonse yochitika ndipo adzasindikiza izi asanapite masiku 30 utachitika msonkhano.
b. Adzasunga chiwerengero cha mpingo.
c. Adzadziwitsa mpingo zonse zimene mbusa wamkulu akufuna kuti mamembala adziwe.
d. Adzagwira ntchito zonse zimene angapatsidwe ndi mbusa wamkulu.
e. Adzakonza komanso adzapereka malipoti ake mpingo.

***v. Wachiwiri kwa Mlembi (Deputy Secretary)***

Wachiwiri kwa Mlembi adzagwira ntchito izi:

a. Adzakhala wachiwiri kwa mlembi.
b. Adzagwira ntchito zimene angapatsidwe ndi mlembi nthawi ndi nthawi.

***vi. Msungi chuma kapena woyang`anira chuma.***

Msungi chuma adzagwira ntchito izi:

a. Adzasunga chuma chonse cha mpingo komanso adzagwiritsa ntchito chumacho motsogozedwa ndi mbusa wamkulu
b. Adzachita chothekera chonse kusunga mbiri yabwino yakagwiritsidwe ntchito ka chumacho ndi kuwerengera kwake.
c. Adzakhala ndi udindo wokonza malipoti azachuma cha mpingo, komanso ndi kuwapereka ku bungwe la Akulu a mpingo.
d. Adzaonetsetsa kuti kasungidwe kachumacho kakuchitika mnjira yovomerezeka ndi amene amadziwa za kusunga chuma.
e. Adzakhala ndi udindo wokonza dongosolo la zachuma la pa chaka ndipo adzalipereka ku bungwe la Akulu a mpingo.
f. Adzakhala m`khala pa mpando wa Bungwe la za chuma.
g. Adzagwira ntchito zonse zimene angapatsidwe ndi mbusa wamkulu.

**Ndime 13: Misonkhano (Meetings)**

i. Bungwe la Akulu a mpingo lidzakumana kamodzi pa miyezi itatu iliyonse
ii. Bungwe loyendetsa ntchito za mpingo lidzakumana kamodzi pa mwezi.
iii. Msonkhano uli wonse usachitike popanda mbusa wamkulu kapena chivomerezo chake ngati zitatero ndiye kuti cholinga chake cha msonkhano sichabwino.

**Ndime 14: Chuma**

*i. kutsegula akaunti ku banki.*

Mpingo uli wonse ukulimbikitsidwa kutsegula akaunti ku banki ina iliyonse ya chisankho chawo. Mbusa adzakhala wosayina wamkulu. Sikwabwino kusunga ndalama mnyumba mwa membala kapena mbusa.

*ii. Chakhumi cha mpingo.*

Mpingo uli wonse udzapereka cha chikhumi chake mwezi uli wonse ku ofesi ya chigawo (District). Mpingo uli wonse umene udzalephera kupereka cha chikhumi chake kwa miyezi itatu mchaka chiri chonse Bungwe loyendetsa ntchito za mpingo wa pamalo lidzapereka chilango ndi atsogoleri oyenera.

*iii. Utumwi.*

Assembly for All Nations ndi mpingo wa utumwi. Tsono mpingo uli wonse udzachita chotheka nthawi zonse kupereka 5% ya zopereka za pa mpingopo mwezi uli wonse ku ofesi ya chigawo chachikulu (Division).

*iv. Tsiku la Utumwi*

Sabata iliyonse yoyamba ya mwezi idzakhala tsiku la utumwi ndipo chopereka cha utumwi chidzalandilidwa.

*v. Maphunziro a Ubusa*

Sukulu ya maphunziro a ubusa ndi yofunikira kwambiri mu Assembly for All Nations. Ntchito yawo iyenera tsono kuthandizidwa ndi mipingo, chifukwa chake mpingo uli wonse uyenera kupereka 5% ya ndalama zake pa mwezi ku sukulu ya ubusa ya All Nations Bible College (ANBC).

*vi. Ndalama zosungira abusa atapuma (Minister`s Benefit Fund)*

Ndalama izi zimasungidwira abusa kuti adzalandire atapuma pa utumiki. Tsono mpingo wonse wa pa malo uyenera kupereka gawo lake kuthumba limeneri kolingana ndi gawo 9, Ndime 3 ya malamulo a akulu amayendedwe a Assembly for All Nations.

*vii. Bungwe la zomangamanga.*

Bungwe la zomangamanga liri ndi udindo wopeza ndalama zothandizira kumanga likulu la mpingowu ku Lilongwe. Mpingo uli wonse tsono udzapereka 2% kuthumbali mwezi ndi mwezi.

## GAWO 4

## Akazi a Abusa

Mkazi wa abusa adzathandizira utumiki wa mwamuna wake. Adzakhalanso monga mlangizi wa utumiki wa amayi pa mpingo. Mamembala a mpingo adzapereka ulemu kwa Mayi Busa monga momwe amaperekera kwa abusa. Komanso Mai Busa akuyembekezeka kukhala mwa ulemu ndi mpingo posakangana nawo. Mayi Busa akuyembekezeka kuchita maphunziro a chaka chimodzi kusukulu ya Baibulo.

Ngati mkazi wa m'busa wamkulu ndi mtumiki wozindikirika pa yekha ndipo ali ndi makalata a utumiki, angathe kusankhidwa kukhala m'busa wothandizira koma osati wogwira ntchito limodzi ndi mbusa wamkulu. Koma adzasiya kukhala wothandizira ngati mwamuna wake atapatsidwa chilango kapena wasunthidwa kupita ku mpingo wina. Koma ngati mwamuna wake wamwalira amene anali m'busa wamkulu iye adzapitilira kukhala mbusa wothandizira pa mpingopo.

## GAWO 5

## Malamulo Achikhalidwe

**Ndime 1:** Ndime iyi iwerengdwe limodzi ndi zimene zalembedwa mu Gawo 18 ndi 19 a mayendedwe a Assembly for All Nations (International constitution). Tsono apa tikufotokozera zimene mwina sizinalembedwe momveka bwino m`magawowa.

**Ndime 2:** Tsono malamulo achikhalidwe ndi akalozera ndi miyezo yoyenera chikhalidwe choyenera ma membala a Assembly for All Nations. Dziko liri lonse, dera liri lonse liri ndi chikhalidwe chake chosiyana ndi kwina. Koma pali chikhalidwe cha chikhirisitu chimene chimafanana ndi cha Khristu. Chimaonetsa kudzipereka kwathu kwa Mulungu posalabadira kusiyana kwa zikhalidwe. Tsono kuphwanya mwadala malamulo achikhalidwewa chingathe

kukhala chifukwa chokwanira kupatsidwa chilango. Bungwe loyendetsa ntchito za pa mpingo ndi limene lidzagamula ngati ndipofunika kupatsidwa chilango kapena ayi.

**Ndime 3:** Zina zimene zingabweretse chilango ndi kukhala ndi khalidwe Losayenera ndi moyo wa chidetsa. Zina mwa izo ndi izi:

i. Kumenya mkazi.
ii. Kukonda kutenga ngongole
iii. Kulephera kubweza ngongole
iv. Kukonda kupemphapempha
v. Kufunsira ndi kukodwa ndi munthu yemwe akumpatsa uphungu
vi. Kusasunga chinsinsi
vii. Kusadziweruza bwino pa khalidwe losayenera la chiwerewere
viii. Kuchita mijedu ndi kunamizira ena pa zinthu zimene sadachite.
ix. Utapezeka kuti wachita chigololo kapena maonekedwe achoipa monga kupezeka malo olakwika, ndi nthawi yolakwika ndi mkazi kapena mwamuna (1 Atesalonika 5:22); kuchita zinthu zimene zingaoneke kuti si zaulemu pa mkazi kapena mwamuna monga: kugwira mawere, ntchafu, maliseche kapena kukakamiza mkazi kapena mwamuna kuchita zinthu zosayenera.
x. Kupezeka wolakwa ndi bwalo la milandu la dziko
xi. Kukhala membala wa magulu a chinsinsi
xii. Kuchita katangale mu mpingo kapena kunja kwa mpingo
xiii. Kulephera kupereka chakhumi miyezi itatu mchaka chilichonse.

**Ndime 4: Mbusa wa mpingo wa pamalo wosamvera Atsogoleri a mpingo**

Mbusa wa pamalo ayenera kudzudzulidwa ndi Dera, chigawo, chigawo chachikulu chifukwa chosamvera atsogoleri nthawi zonse komanso kukana kusunthidwa ngakhale chiyanjano cha mpingo ndi mbusayo chatha. Komanso kusakula kwa mpingo mbusayo atakhala pa mpingopo zaka zisanu (5) kapena kupitilira pamenepo.

**Ndime 5: Mamembala a mpingo wa pamalo wosamvera Atsogoleri a mpingo.**

Mamembala a mpingo angayikidwe pa chilango chifukwa cha zifukwa izi:

i. Kuukira
ii. Kusakhala ndi umwini
iii. Kudzudzula atsogoleri mopanda ulemu.
iv. Kukana kumvera uphungu wa atsogoleri.
v. Kufuna kuchotsa mbusa pa mpingo mopanda kutsata malamulo ampingo
vi. Kuchitira atsogoleri mwano m'malankhulidwe kapena m`machitidwe.
vii. Kupanga magawano mu mpingo.
viii. Kuyambitsa zipolowe mu mpingo kapena kunja kwa mpingo.
ix. Kutsutsana ndi zikhulupiliro za Assembly for All Nations.

**Ndime 6: Kugwiritsa Ntchito Nyumba Ya Mulungu Molakwika.**

i. Kugwiritsa ntchito nyumba ya Mulungu pa ntchito za malonda kapena zina zomwe zikhonza kunyozetsa zina la yesu.
ii. Kulekerera nyumba ya Mulungu osayisamala

**Ndime 7: Kuphwanya khalidwe loyenera mkhristu.**

i. Membala achite ubwino kwa mbusa amene wabwera wakale atasuntha kupita ku mpingo wina.
ii. Membala asanyoze ntchito ya mbusa watsopano poyerekeza ndi ntchito ya mbusa amene wachoka.
iii. Membala asanenerere za ubwino wa mbusa wina kuti abwere pa mpingopo.
iv. Membala asayambitse magulu mu mpingo.
v. Membala asayambitse kuukira mbusa pa mpingo.
vi. Membala asanyoze membala mnzake mu mpingo.

## CHIGAWO 6

### Chilango (kolingana ndi Gawo 19 la mayendedwe)

**Ndime 1: Mtundu ndi cholinga cha chilango**

Chilango chimaperekedwa kolingana ndi mau a Mulungu ndipo mpingo udindo wake ndi kupereka chilangocho. Cholinga choperekera chilango ndicho kuti mulungu alandire ulemu, chiyero ndi ubwino wa utumiki zisungike komanso kuti iwo amene alandira chilango alape ndi kubwezeretsedwanso.

Chilango chiziperekedwa ndi cholinga chofuna kubwezeretsa mtumiki kapena membala komanso kuteteza uzimu wa mpingo. Chilango chizithandiza kupulumutsa komanso kukonza ndipo chiperekedwe ndi chifundo chonse.

**Ndime 2: Ndondomeko ya chilango cha membala pa mpingo.**

i. Bungwe la adindo woyendetsa ntchito za mpingo wa pamalo (Local Assembly Board of Administration) lizaweruza milandu ya mamembala a pa mpingo ndipo lidzapereka chilango kolingana ndi malamulo ndi mayendedwe a Assembly for All Nations.
ii. Ndipo ngati membala sanakhutitsidwe ndi chigamulo cha bwalo la pa mpingo, woyimbidwa mulandu kapena wodandaula ali ndi ufulu wochita apilo kubwalo la Dera (Cluster). Milandu yotereyo idzazengedwa ndi bwalo losankhidwa kuti likamve mlanduwo. Mabwalowa akhalepo wa Dera komanso chigawo kuti adzimva milandu imene yachitidwa apilo.

**Njira yosankhira mabwalo a Apilo.**

i. Bungwe la Adindo oyendetsa ntchito za Dera (Cluster) kapena za chigawo (District) lidzasankha Abusa awiri amene atumikira nthawi yaitali ndi mamembala awiri okhwima mu uzimu amene ali mu delaro kuti akhale bwalo la Apilo.
ii. Madandaulo amvedwe pasanathe masiku 30 kuchokera tsiku limene adandaulira madandaulowo.
iii. Mabwalo a Apilowa asankhidwe kuti agwire ntchito zaka zinayi mofanana ndi mabungwe oyendetsa ntchito za Dera kapena za chigawo. Mwayi ukhalepo wakuti atsogoleri adziko lonse komanso a chigawo chachikulu alowerere pa milandu imene ndi yovuta imene mabwalo a Dera ndi chigawo sangathane nayo. Koma izi zichitike mofuna kuthandizira basi.
iv. Mulanduwo umvedwe pasanathe masiku 30 kuchokera tsiku lolandira mlanduwo. Ukapanda kuzengedwa pa masiku 30, mwai ulipo wokadandaula kubwalo la pamwamba.
v. Membala ngati wapezeka kuti wapyora malire wokonzedwa achotsedwe mu mpingo wa Assembly for All Nations. Membalayu akachotsedwa sadzapezekanso ndi mwayi wolowa mu mpingo wina wa Assembly for All Nations.

**Ndime 3: Kubwezeretsedwa kwa Membala Yemwe Anachotsedwa**

Ngati membala yemwe anachotsedwa afuna kuti abwererenso mu Assembly for All Nations, chiganizo chomuvomera kubwereranso chidzatengera ngati membalayo, walapa zeni zeni.

Ndipo ngati zili choncho ndondomeko yake idzakhala iyi:

a. Adzalemba kalata yopempha kubwerera.
b. kalatayo idzapita kwa iwo amene anamuchotsa mu mpingo
c. Iwo amene adamuchotsa mu mpingo akadzalandira kalatayo adzamuitana kuti adzalankhule naye momufufuza.
d. Ndipo akadzakhutitsidwa ndi kulapa kwake adzamulandira koma mongoyembekezera chabe kwa miyezi isanu ndi umodzi koma osapitilira chaka chimodzi pa mpingo umene angasankhe. Tsono Abusa apa mpingopo adzapereka maganizo awo kuti alandiridwe kapena ayi.

**Ndime 4: Nthawi ndi zofunikira pa chilango cha Membala**

i. Nthawi yobwezeretsedwanso sidzapitilira miyezi isanu ndi umodzi pokhapokhapo uchimowo umakhudza chigololo cha anthu apa bannja, amene saali pa banja, mwamuna ndi mwamuna mnzake kapena mkazi ndi mkazi mnzake, kapena kugonana ndi nyama kapena mwana wobereka wekha ndi zina zotere. Zikatero chilango chake chidzakhala cha miyezi yopitilira isanu ndi umodzi koma osapitilira khumi ndi iwiri.
ii. Membala amene ali pa chilango ayenera kukhulupilika ku misonkhano yonse ya pa mpingo ndi zochitika zina zonse koma sadzatsogolera china chilichonse.

iii. Nthawi ya chilango membala adzaloledwa kudya mgonero chifukwa iye ndi wobadwanso mwatsopano ndipo ayenera kukhala pa chiyanjano ndi abale mwa Ambuye komabe ayenera kuonetsa mtima wolapa zeni zeni.
iv. Membala aliyense amene ali pa chilango ayenera kupereka chachikhumi chake ku mpingo.
v. Tsono zitachitika kuti membalayo wamwalira ali pa chilango mwambo wonse wa maliro udzachitika monga wa mkhristu koma padzayenera kufotokozera monga mmene zinthu zinaliri ndi m`baleyo.
vi. Kubwezeretsedwa kwa membala zidzatengera mmene wolakwayo waonetseera kulapa kwake komanso mmene amatengerapo gawo pa zochitika pa mpingopo monga mwa ndime yaing`ono (ii) ndi (iii) pamwambapa.
vii. Maliro a munthu yemwe sanalandilidwe monga membala. Mbusa atayitanidwa ku maliro a munthu yemwe sanali membala mbusa adzatenga mwayi umenewu kuti afikire ena omwe ndi wotayika. Komabe ma membala a mpingo sakakamizidwa kutsogolera monga mmene angachitire ndi maliro a membala. Padzafunikanso kuti zilengezedwe kuti chifukwa chiyani abusa atumikira pa malilopo. Nyimbo zingathe kuimbidwa kapena ai. Zonse zichitike potsata chiganizo cha akulu a mpingo kolingana ndi m`mene zinthu ziliri nthawi ndi nthawi.

## GAWO 7

### Kusintha Kwa Malamulowa

### (Gawo 30 la Malamulo a Assembly for All Nations)

Malamulowa angasinthidwe pa msonkhano waukulu wa onse a Assembly for All Nations woitanidwa mwanjira yake, maganizo wofuna kusintha atayamba aperekedwa ndi mlembi wamkulu pa kalata ku misonkhano ya chigawo kudzera ku chigawo chachikulu miyezi itatu msonkhano waukulu wa onse usanafike. Kuti kusinthako kuchitike anthu awiri pa atatu ali onse amene ali pa msonkhano adzayenera kuvomereza kusinthako pa chisankho.